

KUPEREKA MBIRI YA PULOGALAMU MWACHIDULE

Pulogalamu ya Njira Zabwino Zophikira Pogwiritsa Ntchito Nkhuni/Makala mu Africa

Mawu Oyambira

Pulogalamu ya “Njira Zabwino Zophikira Pogwiritsa Ntchito Nkhuni/Makala mu Africa” iyambitsidwa ndi cholinga chofuna kuchotsa mbaula za chikale zomwe sizithandiza moyenera ndi kubweretsa mbaula zopindulitsa zamakono ku mabanja akumidzi m’maiko ochuluka muno mu Africa. Izi zikwaniritsidwa ndi pulogalamuyi ikayamba kugwira ntchito zake zogawa mbaula zamakono za mtundu wa ECOA zomwe zimagwiritsa ntchito makala komanso nkhuni.

Cholinga ndi Luso la Pulogalamu

Kugwiritsa ntchito mitengo pophikira kuli ndi zotsatira zoipa zambiri ku chilengedwe chifukwa kumalimbikitsa kuononga nkhalango, nthaka kukokoloka, kuchulukitsa utsi mlengalenga womwe umabweretsa kutentha, kuthetsa chonde m’nthaka, komanso kuchepetsa kuthekera kwa nthaka kusunga madzi. Kuonjezera apo pamene tikuphikira m’nyumba, utsi wochokera nkhuni ndi makala ndi woipa ku umoyo wa munthu chifukwa umabweretsa matenda osiyanasiyana monga Chibayo, kubanika popuma, matenda oumitsa ziwalo, matenda a mtima komanso khansa ya m’mapapo.

Motero, Kampani ya Effective climate solutions 1 FCZO ndi makampani othandizana ake yakhazikitsa dongosolo lofuna kuthandiza pulogalamuyi ndi cholinga chakuti mabanja aku Malawi apeze nawo mwayi ogwiritsa ntchito zipangizo za makono komanso ikufuna kuthetsa mavuto amene amabwera ku chilengedwe ndi umoyo wa anthu tikamagwiritsa ntchito mowirikiza nkhuni/makala pophikira ngati m’mene zilili pano.

Pulogalamu imeneyi isakha gulu la athu oti apindule pa zochitika zake makamaka makomo omwe amagwiritsa ntchito nkhuni/makala ngati njira yokhayo yodalirika pophikira. Pulogalamuyi ibweretsa mbaula za bwino zosunga moto zogwiritsa ntchito makala komanso nkhuni pa mtengo wozizira kuti zilowe m’malo mwa mbaula zachikale. Kotero, mitengo isungika pamene tikuphika komanso tichepetsa kuika utsi mlengalenga omwe umabweretsa kutentha. Kutsogoloku pulogalamu imeneyi izaonjezera ukadaulo wa mbaula ndi njira zina zothetseratu kugwiritsa ntchito mitengo pophikira.

Zonse zizalumikizidwa ndi kampani ya Effective Climate Solutions 1 FCZO ndi makampani othandizana ake omwe akuyang’anira zochitika za pulogalamu imeneyi potsatira njira ya Gold Standard yomwe ndi "KULETSA KUFALITSIDWA KWA UTSI WOIPA: Ukadaulo ndi Njira Zomwe Zimaletsa Kugwiritsa Ntchito Mphamvu Zophikira Zachikale (TPDDTEC) v4.0."

Anthu atenga nawo mbali muzochitika za pulogalamuyi mozipeleka. Ntchito yoyamba ndi kugawa mbaula kwa mabanja m’Malawi, Nigeria ndi Madagascar, komwe misokhano ya anthu okhuzidwa yakonzedwa kuti ikachitike.

M’mene Pulogalamu Izigwirira ntchito Zake

Zochitika mu pulogalamu imeneyi ndi zovomelekezeka ndi ndondomeko zoyenera za Gold Standard for the Global Goals; "KULETSA KUFALITSIDWA KWA UTSI WOIPA: Ukadaulo ndi Njira Zomwe Zimaletsa Kugwiritsa Ntchito Mphamvu Zophikira Zachikale (TPDDTEC) v4.0."

Komwe Pulojeketi Ikuchitikira – Pulojeketi imeneyi ikuchitika m’maiko osiyana-siyana okwanira 48 motere;

Angola	Djibouti	Lesotho	Senegal
Benin	DRC	Liberia	Seychelles
Botswana	Equatorial Guinea	Madagascar	Sierra Leone
Burkina Faso	Eritrea	Malawi	Somalia
Burundi	Eswatini/Swaziland	Mali	South Africa
Cabo Verde	Ethiopia	Mauritania	South Sudan
Cameroon	Gabon	Mozambique	Sudan
Central African Republic	Gambia	Namibia	Tanzania
Chad	Ghana	Niger	Togo
Comoros	Republic of Guinea	Nigeria	Uganda
Congo	Guinea Bissau	Rwanda	Zambia
Cote d'Ivoire	Kenya	Sao Tome & Principe	Zimbabwe

Anthu Osakhidwa – Makomo omwe akugwiritsa ntchito mbaula za chikale zogwiritsa ntchito nkhu

Mgwirizano wa chithandizo – Thandizo lonse ndalama lobwera ku pulogalamuyi lizagwiritsidwa ntchito pa zochitika zake zonse monga m’mene mgwirizano ulili ODA.

Ukadaulo Womwe Waikidwa mu Zochitika za Pulojeketi

Choyambilira cha chochitika cha Pulojeketi ndi kugawa mbaula za mtundu wa “ECO” zomwe ndi za nkhu komanso Makala zomwe zikupangidwa mu Africa muno.



Ecoa Char



Ecoa wood

Mafotokozedwe a Zinthu		
milingo wakagwiridwe ka ntchito	ecoa yogwiritsa nkhu	ecoa yogwiritsa makala
Kuchita Bwino kwa Kutentha	53.7%	71.3%
Mphamvu Yophikira (kW)	1.228kW	0.956kW
PM2.5 pa mphamvu yothandiza yoperekedwa (mg/MJd)	210.2 mg/MJd	38.16 mg/MJd
CO pa mphamvu yothandiza yoperekedwa (mg/MJd)	5.50 g/MJd	3.78 g/MJd
Chidindo Choteteza	97.5%	90%

Zochitika za pulojeketi imeneyi izatenganso mbaula zina zomwe ndi mitundu ina zomwe zimatsatira ndondomeko ya Gold Standard- TPDDTEC V.4.0 ngati amene akuyang'anira ntchitoyi avomeleza.

Ndondomeko ya Pulojeketi

- Kupanga ndi Kukambilana zochitika za Pulojeketi – March – April 2025
- Misokhano wa anthu okhuzidwa – March – May 2025
- Kafukufuku wa m'mene zinthu zilili pano – March 2025
- Kalembera wa anthu/makomo otenga nawo mbali – October 2025

Kugawa kwa mbaula kuzachitika kwa anthu/makomo okhawo omwe asakhidwa.

Thandizo Lobwera Posamala Chilengedwe

Kuchepetsa kuchulukitsa utsi mlengalenga womwe umabweletsa kutentha kumathandiza kusamala chilengedwe. Kotero, pulogalamu izakhala ndi kuthekera kopeza chithandizo cha chuma ngati malamulo ndi ndondomeko zonse za Gold Standard zatsatilidwa moyenerera.

Thandizo la chuma lomwe limabwera posamala chilengedwe limathandiza munjira zambiri monga;

- a) Kugawa mbaula za makono pa mtengo wotsika kuti aliyense athe kugwiritsa ntchito mbaulazi.
- b) Kukuza pulogalamuyi kuti ifikire anthu ambiri
- c) Kubweretsa mwayi wa ntchito kwa nzika
- d) Kulimbikitsa kafukufuku komanso kupanga mbaula za makono pa mtengo wotsika
- e) Kupeleka upangiri wodalarika ndi kukonza mbaula pamene zikugwiritsidwa ntchito.
- f) Kulimbikitsa ndi kudziwitsa anthu ubwino wa mbaula zamakono komanso m'mene angazigwilitsire ntchito.

Ubwino wa Pulogalamu

Mbaula izi zimachepetsa kugwiritsa ntchito nkhu zambiri, kuthandiza umoyo wabwino ndi kusamalira umoyo

wathu wa tsiku ndi tsiku, komanso kukweza chuma cha pakhomo pamene tikugwiritsa ntchito nkhuhi/makala ochepa.

Pweya woipa omwe umachokera mu mbaula zachikale umapeleka chiopsezo chachikulu pa umoyo wa munthu. Pamene mpweya umenewu ukutulutsidwa tili m'nyumba umayambitsa matenda osiyana-siyana monga chibayo, matenda a mtima, matenda oumitsa ziwalo, kubanika popuma, komanso khansa ya mapapo.

Pulogalamuyi, ithandizanso kuchepetsa kudula mitengo mochuluka yopangira nkhuhi/makala.

Ubwino ku Chilengedwe:

Pulogalamuyi ichepetsa kugwiritsa ntchito mphamvu zochokera ku chilengedwe chosabwerezedwa zomwe timagwiritsa ntchito tikamaphika pa mbaula. Motero, kudulidwa kwa mitengo mochuluka ndi cholinga kuti tipangire makala kapena nkhuhi kuzachepa. Kuonjezerapo, kuchepetsa kugwiritsa ntchito mphamvu zochokera ku zachilengedwe zosabwerezedwa (nkhuhi/makala) pophikira kuzapangisanso kuti kutulutsa utsi woipa wamitundu yosiyanasiyana monga NOx, SOx, PM 2.5/10, CO ichepe. Motero, tizankhala ndi m'pweya wabwino pamene tikuphikira m'nyumba. Kugwiritsa ntchito zipangizo za makonozi zithandiziranso kuchepetsa m'pweya woipa omwe umapangitsa kusintha kwa nyengo, motero mavuto omwe amadza chifukwa chositha kwa nyengo azachepanso.

Ubwino ku Chikhalidwe ndi Chuma:

Ukadaulo wa mbaula ndi woti umasunga nthawi, Ubwinowu ndi waukulu kwa amayi ndi atsikana omwe amatenga gawo lalikulu posaka/kutola nkhuhi, komanso pophika. Mbaula zimenezi zipeleka mwayi wogwira ntchito zina zobweretsa chuma pakhomo, komanso nthawi yowerenga za m'kalasi kwa atsikana. Ku nkhuhi ya za chuma, pulogalamuyi ipeleka mwayi wa geni ku mabizinesi ang'ono-ang'ono, kotero kubweretsa mwayi wa ntchito ku malo omwe kuzipezeka mbaulazi.

Kuthandizira ku Mfundo Zachitukuko Chokhazikika



Kupatula kuchepetsa kuika utsi mlengalenga womwe kusokoneza nyengo pobweretsa kutentha kwambiri, pulogalamuyi ikugwirizana ndi zolinga za bungwe la United Nations mu mfundo zachitukuko chokhazikika (Sustainable Development Goal) ya nambala khumi ndi zitatu (13) "Kupanga changu pokhazikitsa mfundo zolimbana ndi kusintha kwa nyengo". Pulogalamuyi ithandiza kulimbikitsa umbwino ma banja akumudzi, anthu ochita businesi zing'onozing'ono komanso ku chilengwedwe mu nthawi yaitali. Zochitika mu pulogalamuyi zithandiza mfundo zachitukuko zokhazikika mu njira izi:

Kuchepetsa kugwiritsa ntchito ndalama zambiri zogulira nkhuhi / Makala

-M'mene mbaulazi azipangira zithandiza kuti nthawi yomwe timaononga pofuna nkhuhi/makala ichepe, popeza zimagwiritsa ntchito makala/nkhuhi mosamala. Kotero anthu azakhala ndi nthawi yambiri yopanga zinthu zina zopezela chuma monga kuchita ntchito za ulimi. (Izi zikugwirizana ndi Mfundo ya Chitukuko Chokhazikika yoyamba (1) ndi ya chisanu (5) (Kuthetseratu umphawi wantundu wina uliwonse, kulikonse, komanso Kukwaniritsa ndondomeko za kusasankhana pakati pa amayi ndi abambo ndikuwapatsa amayi ndi atsikana mwayi wodziyimira pawokha).

- Kuchepetsa Utsi woopsa wa kaboni monokisaidi pamene tikuphikira m'nyumba zomwe zizapangitsa kuchepa kwa matenda omwe amadza chifukwa cha utsiwu monga matenda ovutika popuma, Mutu ndi kuyabwa kwa maso makamaka kwa amayi ndi atsikana omwe amatenga gawo lalikulu pophika pakhomo. (Izi zikugwirizana ndi cholinga chachitatu (3) cha mfundo zachitukuko chokhazikika - Kupititsa patsogolo umoyo wabwino wa anthu onse komanso cholinga cha chisanu (5) - Kukwaniritsa ndondomeko za kusasankhana pakati pa amayi ndi abambo ndikuwapatsa amayi ndi atsikana mwayi wodziyimira pawokha).

- Mbauila za makono izi zimaphika mwachangu kuposa za mbauila za chikale ndipo zogwiritsa ntchito nkhuhi/makala ochepa. Kotero atsikana azakhala ndi nthawi yambiri yochita maphunziro m'malo motaya nthawi yawo pophika. (Izi ikugwirizana ndi cholinga chachinayi (3) cha mfundo zachitukuko chokhazikika, Kulimbikitsa ndi kupititsa patsogolo mwayi wamaphunziro abwino kwa wina aliyense)

- Kuchulukitsa kupezeka kwa luso la makono ndi lodalirika lophikira. (Izi zikugwirizana ndi cholinga cha chisanu ndi ziwiri (7) cha mfundo zachitukuko chokhazikika Kuwonetsetsa kuti anthu onse akupeza mphamvu yodalirika, yokhazikika, yamakono ndi yotsika mtengo komaso kulimbikitsa kuzindikiritsa anthu kudziwa ubwino womwe umakhalapo wotetezedwa ku matenda, Kuthandizira chuma cha pakhomo, komanso phindu ku chilengedwe. Izi zikugwirizana ndi mfundo ya chinayi (4) kulimbikitsa ndi kupititsa patsogolo mwayi wamaphunziro abwino kwa wina aliyense)

- Ndi chithandizo chochokera ku Efficient Climate Solutions, BURN ibweretsa mbaula za zogwiritsa ntchito nkhuhi/makala kuchokera ku Kenya. Izi zithandiza anthu kupeza ntchito zosiyanasiyana m'maiko omwe kuli pulogalamuyi. Zina mwa ntchito zomwe zipezeke ndi zogulitsa mbaula, kuitanira malonda, komanso kugawa mbaula. Pakhalanso maphunziro omwe athandize anthu akumudzi kupeza gawo lodziwa zinthu. Izi zikugwirizana ndi mfundo ya yooyamba (1) - Kuthetseratu umphawi wamtundu wina uliwonse, kulikonse komanso Cholinga cha chisanu ndi zitatu (8) - Kupititsa patsogolo chuma ndi kupezetsa ntchito zabwino zokhazikika kwa anthu onse.).
- Kuchepetsa kudula mitengo mwa chisawawa, kusamalira nkhalango zonse, kubwezeretsa nkhalango zowonongeka m'madera omwe amagwiritsa ntchito mphamvu zosabwerezeka zochokera ku nkhuhi kapena makala. Izi zithandiza kuti chilengedwe sisungike bwino komanso kuthandiza za chilengedwe zopezeka m'mapiri, kusungika kwa madzi komanso nthaka. Izi zikugwirizana ndi mfundo ya khumi ndi zisanu (15) - Kuteteza, kubwezeretsa, ndi kulimbikitsa kagwiritsidwe ntchito ka za moyo za pa mtunda ndi kusamala nkhalango, kuthetsa chipululu ndi kuwonongeka kwa nthaka)

Kutsatira mfundo za ndondomeko ya Chitetezo

Kuwunikira mokwanira mfundo za dongosolo ya chitetezo kuchitika pofuna kutsatira malamulo a chitetezo a Gold Standard, komanso kulemekeza malamulo a dziko la Malawi, chikhalidwe, komanso malamulo onse a m'dera. Mfundo zikulu-zikulu zoyenera kutsatira zalembedwa munsimu mwa chidule motere;

Mfundo za Chikhalidwe cha Anthu

- **Mfundo yoyamba:** Ufulu wa Chibadwidwe: Kugawa kwa mbaula za makono kapena zochitika zili zonse zili mu pulogalamu imeneyi kulibe kuthekera kwakuti kutha kuphwanya ufulu wa chibadwidwe, kapena malumbiro a maiko olimbikitsa ufulu wachibadwidwe. Zonse ziyenda monga imakambila mfundo za dongosolo la chitetezo a Gold Standard for Global Goals. Pa nthawi imene kuzakhale msonkhano wa anthu okhuzidwa mu pulogalamuyi, anthu a ku Kampaniyi azafotokozera onse oitanidwa m'mene malamulo a maiko, m'dziko, kapena m'dera angazatsatidwire mwa ntchuntchu.
- **Mfundo ya Chiwiri:** Kupereka mwayi kwa anthu a m'dera mofanana kusatengera kuti ndi wamwamuna kapena wamkazi ndi kupeleka mphamvu kwa amayi: Kugwiritsa ntchito zipangizo za makono ngati m'lowa-malo mwa zipangizo za chikale kuchepetsa kugwiritsa ntchito makala/nkhuhi zambiri zomwe zili ndi ubwino kwa amayi. Ubwinowu uzapelekedwa bwino bwino pa tsiku la msonkhano wa athu onse okhuzidwa mogwirizana ndi cholinga cha chisanu cha mfundo cha chitukuko chokhazikika.
- **Mfundo ya Chitatu- Umoyo wa M'dera ndi Chitetezo:** Palibe chiopsezo chili chonse choononga umoyo

wa m’dera pamene zochitika za pulogalamu zayamba. Oyendetsa ntchito imeneyi azaonetsetsa kuti zochitika zake zonse zikulumikazana ndi anthu powafotokozera za ndondomeko zonse za chitetezo, komanso ndondomeko zotetezera ogwira ntchito kwa anthu amene alembedwa muzochitika za pulogalamu imeneyi.

- **Mfundo ya Chinayi: Chikhalidwe cha anthu, Mbadwa za M’dera, Kuthamangitsidwa kapena kusamutsidwa:** Cholinga cha pulogalamu ndi kukhazikitsa zipangizo zophikira za makono, kotero palibe chiopsezo chakuti itha kazaononga kapena kusokoneza chikhalidwe anthu. Otsogolera pulogalamu azaonetsetsa kuti zochitika zake zikutsatira zofunikira zonse. Anthu onse okhuzidwa azauzidwa mfundo zonse za chitetezo monga;

-Kuteteza malo a chikhalidwe cha anthu komanso osasokoneza mbiri yake

-Kupewa kuthamangitsidwa kapena kusamutsidwa kwa nzika za m’dera.

-Malamulo okhuza malo ndi ufulu wina uli wonse

-Ufulu wa mbadwa za m’dera.

- **Mfundo ya Chisanu: Ziphuphu:** Otsogolera Pulogalamu izaonetsetsa kuti zochitika zake sizikulimbikitsa ziphuphu komanso anthu akufotokozeredwa za kuipa kochita ziphuphu komanso kuuzidwa kuti BURN sizalekerera mtundu uli wonse wa ziphuphu pamene ntchito za pulogalamu zokhazikitsidwa.

- **Mfundo ya Chisanu ndi Chimodzi:** Zotsatira za Chuma: Pulogalamu izalemekesa ufulu wa anthu ogwira ntchito. Sizalekelera mchitidwe ogwiritsa anthu ntchito mwa ukapolo kapena kuphwanya malamulo a ntchito ovemelekezeka ndi maiko. Zochika zonse zizatsata mfundo ya chisanu ndi chimodzi yoyenera mu Gold Standard Safeguarding Principles.

Chilengedwe ndi Ubale wa Zolengedwa Zonse

Mfundo ya chisanu ndi ziwiri: Nyengo ndi mphamvu za Chilengedwe

- **Kuika Utsi mlengalenga:** Pulogalamu ichepetsa kuika utsi mlengalenga omwe umasokoneza nyengo kuchokera mmene ulili pano ndi kufika zaka khumi ziwiri zikubwerazi. Luso lomwe laikidwa lithandiza kupewa kuika utsi wambiri wa kaboni daiokisaidi mlengalenga.

- **Mphamvu Zachilengedwe:** Cholinga cha pulogalamu kukhazikitsa luso la makono logwiritsa ntchito mphamvu zochokera ku zachilengedwe zosabwerezeka zochepe po phikira. Motero, kuchuluka kwa mitengo yodulidwa kuchokera nkhalango kuzachepa kusiyana ndi m’mene zili pano.

Mfundo ya chisanu ndi zitatu: Madzi

- **Zotsatira za kuyenda kwa Madzi:** Pulogalamu sizaonga madzi, kusokoneza m’mene madzi amayendera, komanso kupangitsa makomo kuti asowe madzi kapena kukokoloka kwa nthaka.

- **Kukokoloka Kwa Nthaka:** Pulogalamu ichepetsa kugwiritsa ntchito nkhu ni kotero iteteza nkhalango. Pa chifukwa chimenechi, kukokoloka kwa nthaka kuzachepa ndipo madzi sazayenda mothamanga.

- **Mfundo ya chisanu ndi zinayi:** Chilengedwe, Ubale wa zolengedwa, ndi kagwiritsidwe ntchito ka malo
- **Kugwiritsa Ntchito Malo kapena Nthaka:** Palibe mbewu iliyonse yomwe ingazalidwe ngati gawo limodzi la pulogalamu imeneyi.
- **Chiopsezo ku Ngozi ya chilengedwe:** Palibe zotsatira zili zonse zomwe pulogalamu ingathandizire kubweretsa ngozi ya chilengedwe.
- **Kubweretsa Mbewu za Genetiki:** Palibe kugwiritsa ntchito mbewu kapena zinthu zopangidwa mwa Genetiki zomwe zimaopseza chilengedwe.
- **Kutulutsa zonyasa zoononga Chilengedwe:** Malingana ndi zochitika za pulogalamu, kugwiritsa ntchito nkhuhi/makala kuzachepa, kotero palibe kugwiritsa ntchito mafuta ambiri ochokera kuzotsalira zachilengedwe. Motero, palibe chiopsezo chotulutsa zonyasa zomwe zimaononga chilengedwe.
- **Kutaya zinyalala ndi zina zoopsa:** Panthawi yopanga mbaulazi, pulogalamu izagwira ntchito ndi makampani a m'dera ndipo izatsata malamulo oteteza kutaya zinyalala ndi zina zoopsa ku chilengedwe. Pulogalamu izakhazikitsa ndandanda wabwino wa m'mene zinyalala azisamalira mu nthawi yonse imene ikugwira ntchito
- **Fetereza ndi Mankhwala Ophera Tizilombo:** Palibe njira ina iliyonse yomwe Pulogalamu ingazagwiritse ntchito fetereza kapena mankhwala ophera tizilombo m'munda pa zochitika za ntchito zake.
- **Kukolola Mitengo:** Pulogalamu ichepetsa kufunikira kwa mitengo pophikira kotero iteteza nkhalango zanthu m'dziko muno.
- **Chakudya:** Pulogalamu ilibe chiopsezo pa chakudya kapena kusokoneza kulima kwa chakudya.
- **Ulimi wa Ziweto:** Pulogalamu sikukhuzana ulimi wa ziweto.
- **Kusamala za chilengedwe zosiyana-siyana m'malo ake:** Ntchito ina iliyonse ya pulogalamu izayenera kusonyeza kuti ikutsata ndi kuteteza za chilengedwe zonse m'malo ake molingana ndi malamulo a dziko komanso ndondomeko zomwe maiko onse oyenera kutsata.
- **Zolengedwa zomwe zili pa Chiopsezo:** Pulogalamu ilibe kuthekera koika chiopsezo kapena kusokoneza zolengedwa malo ake. Ntchito zake zizakhala makomo komaso mabungwe.
- **Kubweretsa Mtundu wa chilendo wa mbeu:** Palibe mtundu uliwonse wa mbewu kapena zomera zomwe zizayambitsidwe mu pulogalamu imeneyi

Ndemanga/kupereka maganizo/kufuna kupanga gwirizano

Nathan P.M. Gachugi,

Director of Carbon Operations,

EOA CLIMATE CAPITAL

(project representative)

nathan.gachugi@burnmfg.com

+254 727 423 191